# UNDUNA WA ZACHILENGEDWE NDI KUSINTHA KWA NYENGO

NTHAMBI YOWONA ZANYENGO NDI KUSINTHA KWA NYENGO

**NYENGO MSABATAYI**


**KUYAMBIRA PA 4 MPAKA 10 MARCH, 2024**

## NYENGO M'SABATA IKUBWERAYI

Kuyambira mawa Lolemba pa 4 March kufika Lamulungu pa 10 March 2024, **tiyembekezere nyengo ya mitambo ndipo kugwa mvula ya mabingu m'madera ambiri yomwe igwe ya mphamvu m'madera ochulukirapo makamaka m'madera okwera, am'chigawo cha kumpoto komanso am'mphepete mwa nyanja ya Malawi**. Izi zikhale chonchi kamba ka dera lodzetsa mvula lotchedwa ITCZ. **Chiopsezo chakusefukira kwa madzi chikhala chokwera m'madera ena monga m'madera am'mphepete mwa nyanja ya Malawi, komanso m'madera otsika ndi m'malo omwe kumakonda kusefukira madzi.** Pali kuthekera kwakukulu kwa Namondwe kubadwa munyanja ya m'chere ya India pakati pa dziko la Madagascar ndi Mozambique musabatayi. Pakadali pano, sizinadziwike njira imene Namondweyu angatenge akabadwa.Nthambi ya Zanyengo ndi Kusintha kwa Nyengo ipitiriza kuchita kauniuni wa Namondweyu ndikukudziwitsani momwe atayendere.

## NYENGO MU SABATA YANGOTHAYI

Kunali kwa nyengo ya mvula m'madera ambiri ndipo mvula inagwa ya mphamvu kwambiri m'madera ena monga ku Nkhotakota komwenso madzi anasefukira (Flash Floods) kuyambira pa 27 February, 2024. Mvula ya mlingo wa 475.1mm inayezedwa ku Nkhunga ku Nkhotakota pa 29 February pomwe ya mlingo wa 185.6mm inayezedwa ku Dwangwa m'boma lomwero. Pa 28 February, 2024 mvula ya mlingo wa 215.2mm inayezedwa ku Nkhotakota Met station, pomwe ya mlingo wa 283.1mm inayezedwa ku Nkhunga ndipo ya mlingo wa 126mm inayezedwa ku Dwangwa.




*Mapu: Mvula yomwe inayezedwa kuyambira pa 27 mpaka pa 29 February 2024.*

## MALANGIZO M'SABATALI

- Titsatire mauthenga a Zanyengo mwa chidwi.
- Nthawi zambiri mvula ya mabingu imabwera ndi mphenzi komanso mphepo ya mkuntho, choncho, tibisale malo otetezeka bwino mvulayi ikamagwa.
- Tisaoloke, kapena kuyendetsa galimoto pomwe madzi asefukira kapena akuthamanga kwambiri.
- Tikonze ndi kusamalira ngalande zodutsamo madzi kuti tichepetse chiopsezo chakusefukira kwa madzi.

## UNDUNA WA ZACHILENGEDWE NDI KUSINTHA KWA NYENGO

NTHAMBI YOWONA ZANYENGO NDI KUSINTHA KWA NYENGO

***Kuti mudziwe zambiri funsani kwa:*** *The Director, Department of Climate Change and Meteorological Services, Ministry of Natural Resources and Climate Change, P. O. Box 1808, Blantyre, Malawi. Tel: (265) 882 266 579; Email: metdept@metmalawi.gov.mw , Website: www.metmalawi.gov.mw*


**Malo osindikizira: Blantyre** **Yatulutsidwa Lamulungu pa 3 March, 2024**